NAME:___________________________________ NO.:_____________________

# NORTHEN EDUCATION DIVISION MOCK EXAMINATION

## 2026 MALAWI SCHOOL CERTIFICATE OF EDUCATION

# CHICHEWA

**Subject Numbe: MO32 / III**

**Friday, 27th March** **Time allowed: 2hours**

**8:00-10:00 am**

**PAPER III**

**(Malikisi 70)**

**Malangizo:**

1. Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi ndi limodzi
2. M' gawo **A**: Yankhani mafunso onse **(Malikisi 30)**
3. M' gawo **B**: Yankhani mafunso awiri okha. **(Malikisi 40)**
4. Lembani dzina lanu pamwamba pa tsamba lililonse loyankhirapo
5. Muchitebulo chili kumbaliku onetsani funso lililonse lomwe mwanyakha pochonga mubokosi lomwe lili Kutsogolo kwake.
6. Perekani pepalali kwa oyang' anira mayeso nthawi ikakwana

| Funso | Chongani Funso ngati Mwayakha | Muno musalemde mo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| | | | |



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

NAME:________________________________ NO.:___________________

**Gawo A** (Malikisi 30)

**Nkhani za Mchezo ndi Zolembedwa**

**Langizo:** Yankhani mafunso onse m'gawoli pa mizere ili pansi pa funso lililonse.

1. Werengani ndakatulo ili m'munsimu ndipo muyankhe mafunso otsatirawo pa mizere ili pansi pa funso lililonse

**Mtengo Wosalala (Sam A. Mchombo)**

Poyang'ana kwambiri mtengowu,
Sikudabwa kwake mumtima
Kuti komadi kusalala kotere
Kungakhale pamtengo

Sukuchita kusowa pomwe uli,
Poti inayo njazikang'azikang'a.
Iwo ndi chipatso chakupsa
Pakati pazosapsa

Sikuchita kusowa pomwe wayima
Kuwala kuwalira mitengo yamthuziyo
Mtengo wake uli ngati nyali
Yokola zouluka kholophete

Ulinso ndi zipatso zabwino.
Chipatso chimodzi gwi!



Downloaded for **FREE** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Mkamwa ponyeni,
Kukoma ngati uchi ndithu.

Kudabwadi zedi,
Kuti mtengo woterewu
Udatuluka padothi limodzi?

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa**

(a)Kodi yemwe akuyankhula m'ndakatuloyi ndi ndani?

______________________________________________________

**(Malikisi 1)**

(b) Fotokozani zinthu **ziwiri** zomwe woyankhulayo akudabwa nazo.

(i) __________________________________________________

__________________________________________

(ii) __________________________________________________

__________________________________________

**(Malikisi 2)**

(c)Tchulani mtundu wa ndakatuloyi.

__________________________________________________

**(Malikisi 1)**

(d) Fotokozani tanthauzo lobisika la ndakatulo iyi.

______________________________________________________

______________________________________________________

__________________________________________

**(Malikisi 2)**



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

(e)Perekani zitsanzo za zipangizo izi m'ndakatuloyi.

**(i)** chifanifani

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

(ii) funso lachodziwadziwa

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

(iii) mvekero

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

(f) Perekani matanthauzo a mawu otsatirawa m'ndakatuloyi.

(i) njazikang'azikang'a

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

(ii) udatuluka padothi

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

(iii) Perekani phunziro lomwe likupezeka m'ndakatuloyi

______________________________________________

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

**2. Werengani nkhani ili m'munsimu mosamala ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.**

**CHILOMBO CHOLUSA**



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Tsiku lina m'mudzi mwa Kadole, anthu atangodya mgonero, mudamveka mkuwo woswa makekhutu. Mkuwowu udachokera kunyumba zina zomwe zidali m'mphepete mwa mtsinje wotchedwa Chiwungu.

Chilombo kuno! Chilombo kuno! Dzandithandizeni, ndikufa kuno! Mawu achikazi adamveka motero, uku kulira kwa ana kukumveka chamkatikati! Poyamba anthu ena adanyozera poganizira ndi momwe a Sanasho amamenyera akazi awo akadakwa. Khalidweli anthu adatopa nalo n'chifukwa chake adaganiza kuti tsikulo zidalinso chimodzimodzi. Patapita kanthawi, anthu adayamba kukhamukira kumaloko poona kuti mfuwu udali kunkirankira. Panthawiyi n'kuti tsopano ana onse a pakhomo pa Sanasho atawatsekera m'nyumba ngati nkhuku.

Apa anawo adali akungodzilirira m'nyumbamo ngati kuti mwina kwagwa Chauta. Bambo Sanasho, nthungo ili m'dzanja lamanja komanso chisenga m'dzanja linali, adali pafupi ndi khola lambuzi. Uku thukuta lili kamukamu komanso akunthunthumira. Anthuwo adadziwa kuti pamalopo paterera. Atawafunsa bambowo chomwe chidatsitsa dzaye kuti njovu ithyoke mnyanga, a Sanasho ankangoloza mkhola lambuzilo ndi chisenga koma mawu osatuluka n'komwe ngati athiridwa ufa walipoko kukhosi. Kenako mawu adatuluka mkamwa mwa bamboyu koma modukizadukiza 'chi... chilombo mkholamo... cha... chameza mbuzi yanga yapa...pa...pamtima.

Mnyamata wina wolimba mtima dzina lake Nutwe adapita kufupi ndi kholalo. Adayang'anitsitsa mkholamo nawona chinthu china chikudzithinulathinula. Poyang'anitsitsa adazindikira kuti inali nsato. Anthu adayatsa muuni mwansanga ndipo adaona kuti kukamwa kwake



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

kudali miyendo iwiri ya mbuzi yam'mbuyo. Ichi chidali chitsimikizo choti njokayo idamezadi mbuzi ya bambo Sanasho.

Akuluwa adasweka mtima popeza mbuziyo idali yabere ndipo idali yoti iswa posakhalitsa. Kuonjezera apo, banjali lidalibe pena potsamira koma pa chiweto chokhacho basi. Nsatoyo itadziwa kuti mwana wakana phala, ndipo kuti ikapusa, iyiwala gaga, idayamba kulavula mbuziyo mwachangu pokonzekera kulimbana ndi anthu aja. Apa n'kuti atakonzekera miyala, zibonga komanso nthungo zili mmanja. Mbuziyo n'kuti ili apo lambii komanso ili ndi malovu okhaokha thupi lonse.

Nkhondo idayambika yolimbana ndi nsato. Ena uku akuyigenda ndi miyala, ena ndi zibonga komanso ena akuyilasa ndi nthungo. Padalidi fumbi koboo! Popeza nayo njokayo, idafuna kudzipulumutsa kwa adani ake popeza mwamuna mnzako mpachulu umalinga utakwerapo. Mathero a nkhondoyi sadali kudziwika.

Madodawa ndi anyamata sanafune kuipatsa mpata nsatoyo koma kuyikong'ontha mpaka pang'onopang'ono idayamba kufooka. Padatenga pafupifupi ola latunthu nkhondo ili mkati. Pamapeto pake, mkulu wina yemwe adali wa luso lauzimba, dzina lake Ndope adangoilasa njokayo pakhosi mwachandamale ndipo idafera pomwepo.

Patapita mphindi zochepa, abambo angapo adasenda chikopa chanjokayo ndi kutumbula pa mimba pake. M'mimba adapezamo bakha yemwe njokayo idameza kumalo kwina. Apa n'kuti amayi akuyimba nthungululu ali lulululu chifukwa chilombocho chidafa. Mmene mkulu wina adafunsa za chikopa chija, n'kuti chitamerapo miyendo kale.



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

NAME:__________________________________ NO.:____________________

Aliyense adali chimwemwe tsaya popeza padalibe ndi m'modzi yemwe adavulazidwa ndi chilombo cholusacho. Kufuna kutsendera chisangalalo a Sanasho adaona kuti chidali chinthu chanzeru kugawa nyama yambuzi yomwe idapulumuka mkamwa mwa nsato ija kwa anthu ofuna kuti akatsuke mkamwa ngati chithokozo pa ntchito yomwe adagwira.

a. Nkhaniyi ikuchitikira kuti?

__________________________________________________________

**(Malikisi 1)**

b. Ndi chifukwa chiyani ana onse adawatsekera m'nyumba?

____________________________________________________________

______________________________________________________

**(Malikisi 2)**

c. Tsimikizani kuti anthu a m'mudzi wa Kadole adali ogwirizana?

____________________________________________________________

______________________________________________________**(Malikisi 2)**

d. Ndi chiyani kwenikweni chidakuza chisangalalo njoka ija itaphedwa?

____________________________________________________________

______________________________________________________**(Malikisi 2)**

e. Tchulani mphendero ya nkhaniyi

___________________________________________________________

**(Malikisi 1)**

f. Perekani zipangizo **zitatu** zomwe zagwiritsidwa ntchito m'nkhaniyi



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**NAME:**____________________________________ **NO.:**______________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

________________________________________________________

**(Malikisi 3)**

g. Tsimikizani kuti Sanasho ndi mpangankhani wosintha

__________________________________________________________________

__________________________________________________________

**(Malikisi 2)**

h. Fotokozani mfundo **imodzi** yomwe yasonyezedwa mnkhaniyi.

______________________________________________________________________

_____________________________________________________________

**(Malikisi 2)**

## GAWO B (Malikisi 40)

**Langizo: Yankhani mafunso awiri okha m'gawoli m'ndime zofotokozedwa bwino.**

### NTHONDO **(S J Nthala)**

3. a. Atengambali ambiri adaonetsa kudalira m'bukhuli. Fotokozani popereka zitsanzo **zinayi** zovomereza mfundoyi.

**(Malikisi 20)**

**KAPENA**



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

b. Tsimikizani popereka mfundo **zinayi** kuti 'mvula ikakuona litsiro

siikata' potengera moyo wa Nthondo .

**(Malikisi 20)**



Downloaded for ***FREE*** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

NAME:________________________________ NO.:___________________

______________________________________________________________

______________________________________________________________

______________________________________________________________

______________________________________________________________

______________________________________________________________

______________________________________________________________

______________________________________________________________

______________________________________________________________

______________________________________________________________

______________________________________________________________

________________________________________________________

## CHAMDOTHE NDI ZISUDZO ZINA

**(S Likongwe, W Nkhoma)**

## CHAMDOTHE

**4.** a**.** Tsimikizani popereka mfundo zinayi zowonetsa kuti kuteteza ndi imodzi mwa  mfundo zikuluzikulu mu chisudzochi.

**(Malikisi 20)**

## KAPENA

## MUDZI WA MFUMU TANDWE

**b.** M'chisudzochi mayi Amuli akufotokoza kuti m'mudzimu anthu samasalana pa zinthu zina. Tsimikizani popereka mfundo **zinayi**.



Downloaded for ***FREE*** from *www.kizitochikuni.com* - For more info: *contact@kizitochikuni.com*

NAME:____________________________________ NO.:______________________

© 2026 NED MOCK



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**NAME:**__________________________________ **NO.:**____________________

________________________________________________________________________

________________________________________________________________________

________________________________________________________________________

________________________________________________________________________

________________________________________________________________________

________________________________________________________________________

________________________________________________________________________

________________________________________________________________________

________________________________________________________________________

________________________________________________________________________

________________________________________________________________________

________________________________

## MAFUNSO ATHERA PANO



Downloaded for **FREE** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com